-Chifukwa chakuti Mulungu anamulonjeza Aburahamu kuti adzatumiza Mpulumutsi kupitira mwa a Isirayeli.



## PHUNZIRO LA 27

1. Kodi Farawo watsopanoyo anachita chiyani kwa a Isirayele?
-Anaŵasandutsa a Isirayele onse kukhala akapolo.

2. Kodi chifukwa chiyani Farawo anaŵasandutsa a Isirayele onse kukhala akapolo?
-Farawo ankawopa kuti a Isirayele angadzalande dziko lake.

3. Kodi chifukwa chiyani Farawo ankawopa kuti a Isirayele angadzalande dziko lake?
-Chifukwa chakuti a Isirayele anachulukana kwambiri.

4. Kodi amene ankamutsogolera Farawo kuti aŵasandutse a Isirayele onse kukhala a kapolo anali ndani?
-Satana.

5. Kodi chifukwa chiyani Satana ankafuna kuŵawononga a Isirayele?
-Chifukwa chakuti Satana ankadziŵa kuti Mulungu analonjeza zutumiza Mpulumutsi kupitira mwa a Isirayele.

6. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaŵadalitsa a Isirayele?
-Chifukwa chakuti Mulungu anaŵakonda a Isirayele.
-Chifukwa chakuti Mulungu sankafuna kuti aphwanye lonjezo Lake kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo.

7. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamutumiza mwana wa mkazi wa Farawo kuti amulele Mose?
-Chifukwa chakuti Mulungu anakonza zoŵatsogolera a Isirayele kupitira mwa Mose potuluka mu Ejipito.

8. Kodi pali munthu amene angayiletse tchito ya Mulungu?

-Palibe.

9. Kodi pali chiwanda chimene chingayiletse tchito ya Mulungu?
-Palibe.

10. Kodi Satana angayiletse tchito ya Mulungu?
-Iyayi.

11. Kodi a Isirayele anakatha kudzipulumutsa okha kwa Farawo?
Iyayi.

12. Kodi Mose anakatha kuŵapulumutsa a Isirayele kwa Farawo?
-Iyayi.

13. Kodi ndi ndani yekha amene anakatha kuŵapulumutsa a Isirayele kwa Farawo?
-Mulungu.

14. Kodi ndi ndani yekha amene angaŵapulumutse anthu kwa Satana?
-Mulungu.

-A Isirayeli anakhala ku Ejipito mu ukapolo kwa zaka 400.

-Chifukwa chakuti a Isirayele ankavutika kwambiri, iwo analilira kwa Mulungu.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 2:23b

23-A Isirayeli ankangolira nawo ukapolo wawo uja, namapenpha chithandizo, ndipo kulira kwawo kunamveka kwa Mulungu.



17-Utenge ndodo yimene yili m'manja mwakoyo, ukachite nayo zozizwitsa ndodo imeneyo."

-Kodi Mulungu anamutumiza ndani kuti akamuthandize Mose kulankhula kwa Farawo?
-Aroni, m'bale wake wa Mose.

-Chifukwa chakuti Mulungu anamulonjeza Mose kuti amutumizira m'bale wake, Aroni, kuti akamuthandize iye, anavomera kupita.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 4:18 ndi20

18-Tsopano Mose anabwera kwa Yetero, mpongozi wake uja namuwuza kuti, "Chonde mundilole kuti ndibwerere ku Ejipito kwa abale anga, kuti ndikaŵawone ngati ali moyo."Yetero adawuza Mose kuti, "Pitani ndi mtendere. "

20-Chomcho Mose anatenga mkazi wake ndi ana ake, naŵakweza pa bulu onsewo, ndipo anapita ku Ejipito, atatenga ndodo imene anamupatsa Mulungu ija.

-Mulungu sanapupulume naye Mose.

-Ngakhale kuti Mose sankafuna kuti akaŵatsogolele a Isirayeli kutuluka mu Ejipito, Mulungu anali atamusankhabe iye.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu ankafuna kuti aŵapulumutse a Isirayeli mu ukapolo.

-Chifukwa chakuti Mulungu anaŵakonda a Isirayeli, ndipo Iye sanafune kuti iwowo akhale mu ukapolo.

-Chifukwa chakuti Mulungu anamulonjeza Aburahamu kuti adzaŵatsogolera iwowo kubwelera ku dziko la Kanani.

-Mulungu.

-Mulungu anamuwuza Mose kuti akamuthandiza iye kulankhula bwino.

-Ngakhale kuti Mulungu ankafuna kuti amuthandize Mose, Mose sankafunabe kuti aŵatsogolere a Isirayeli kutuluka mu Ejipito.

-Tiyeni tiŵerenge zimene analankhula Mose kwa Mulungu:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 4:13

13-Koma Mose adati, “Pepani AMBUYE, ndikukupemphani kuti mutume wina amene angathe kulankhula bwino.”

-Mulungu anamukalipila Mose, chifukwa chakuti ankawopa kuti akaŵatsogolele a Isirayeli kutuluka mu Ejipito.

-Koma Mulungu anamutumiza munthu wina kuti akamuthandiza Mose kulankhula kwa Farawo.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 4:14-17

14-Pompo AMBUYE anamukalipira Mose, namufunsa kuti, “Bwanji m’bale wako Aroni, Mlevi uja? Ndikudziwa kuti angathe kulankhula bwino kwambiri. Iyeyo akubwera kudzakumana nawe, ndipo adzakondwa kwambiri pokuwona.
15-Udzalankhula naye iyeyo ndikumuwuza zakuti akanene. Ndidzakuthandizani kulankhula nonse aŵirinu, ndipo ndidzakuwuzaninso zoti mukachite.
16-Iye adzikalankhula kwa anthu m’malo mwako. Adzakhala okulankhulira, ndipo iwe udzakhala ngati Mulungu ndiwe kwa Aroni.



-Kodi Mulungu anadziŵa zakuti a Isirayeli akuvutika?
-Kodi Mulungu anakumva kulira kwa a Isirayeli?

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 2:24-25

24-Mulungu anamva kudandawula kwawoko, ndipo anakumbukira chipangano chake chija chimene anachita ndi Aburahamu, Isaki ndi Yakobo.
25-Mulungu ataŵapenya a Isirayeliwo, ndipo anaŵamvera chifundo.

-Mulungu anadziŵa kuti a Isilayeli akuvutika kwambiri.
-Mulungu anakumva kulira kwa a Isirayeli.

-Mulungu anakumbukiranso lonjezo limene anapereka kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo.

-Kodi lonjezo la Mulungu kwa Aburahamu, Isaki ndi Ykobo linali litani?

-Lonjezo la Mulungu linali lakuti, pakadzatha zaka 400, Iye adzaŵabwezeretsanso a Isirayeli ku dziko la Kanani.

-Mwina mwake a Isirayeliwo ankaganiza kuti Mulungu wayiwalira iwowo, koma Mulungu sayiwala.

-Nthaŵl zonse Mulungu amachita zimene walonjeza kuti adzazichita.

-Ngakhale kuti Mulungu safulumira, Iye amachita zimene walonjeza kuti adzazichita mu nthaŵl Yake.

-Kodi Mose anali kuti?
-Kodi Mulungu sanakhoze zoŵatsogolera a Isirayeli kupitira mwa Mose potuluka mu Ejipito?

-Kodi Mulungu sanakhoze zoŵatsogolera a Isirayeli kupitira mwa Mose potuluka mu ukapolo?

-Chifukwa chakuti Farawo ankafuna kumupha Mose, Mose anathaŵira ku dziko la Midiya.

-M'dziko la Midiyani, Mose anakwatira ndipo anali ndi ana amuna aŵiri.

-Tsiku lina, Mose akuweta ziweto za apongozi ake, anawona zinthu zozizwitsa.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 3:1-3

1-Mose ankaweta ziweto za mpongozi ake Yetero, wa msembe uja wa ku Midiyani. Tsiku lina anazitenga ziwetozo, nayenda nazo cha ku zambwe kwa chipululu, mpaka kukafika ku phiri la Mulungu dzina lake Horebu.

2-Mngelo wa AMBUYE anamuwonekera ngati malaŵl a moto umene unkayaka m'chitsamba. Mose atapenya anawona kuti chitsamba chili moto laŵilaŵl, koma osapsa.

3-Tsopano mu mtima mwake anati, "Ndipita pafupi, kuti ndikawonetsetse zozizwitsa zimene ndikuziwonazi. Chifukwa chiyani chitsambachi sichikupsa?"

-Kodi Mose anawona chiyani?
-Mose anawona chitsamba chimene chinkayaka, koma sichinkapsa.

-Kodi chifukwa chiyani chitsamba chimene anachiwona Mose chikuyaka chija sichinkapsa?
-Chifukwa chakuti Mulungu anali mchitsambacho.

-Chifukwa chakuti Mulungu anali mchitsambacho, chitsambacho sichinkapsa.



kukhala labwinobwino atalilowetsanso mchovala chakecho.

-Ngakhale kuti Mulungu anamupatsa Mose zizindikiro ziŵirizi, Mose ankawopabe kuti a Isirayeli sakamutsatira iye.

-Apa pali zimene Mose analankhula kwa Mulungu.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 4:10

10-Mose adati, "Pepani AMBUYE, ndapota nanu, ine sindidziŵa kulankhula bwino chiyambire kale, ndiponso kuyambira paja mwayamba kulankhula nane, mtumiki wanune. Lilime langa ndi lolemela, ndine wa chibwibwi."

-Mose anamuwuza Mulungu kuti anali wa chibwibwi ndiye sakatha kulankhula bwino.

-Kodi Mulungu anamuyankha chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 4:11-12

11-Apo AMBUYE anamufunsa Mose kuti, "Kodi amene anamupatsa munthu pakamwa ndani? Kodi ndani amene amasandutsa munthu kuti akhale wosamva kapena wosalankhula, wopenya kapena wosapenya? Kodi sindine AMBUYE amene ndimachita zimenezo?

12-Tsopano pita, ine ndidzakuthandiza kulankhulako, ndipo zoti ukanene ndidzakuwuza ndi INE."

-Kodi ndani amene anamupatsa Mose kulankhula?
-Mulungu.

-Kodi amene anakamuthandiza Mose kulankhula bwino ndani?

4-Apo AMBUYE anamuwuza Mose uja kuti, “Igwire mchira.”Mose adayigwira, pompo idasandukanso ndodo m’manja mwakemo.

5-AMBUYE adamuwuza kuti, “Ukachite zimenezo ndipo adzakukhulupilira kuti AMBUYE, Mulungu wa makolo awo, Mulungu wa Aburahamu, Mulungu wa Isaki, Mulungu wa Yakobo, adakuwonekeradi.”

6-AMBUYE anamuwuzanso Mose kuti, “Tapisa dzanja lako m’malayamo.”Iye adapisadi. Koma potulutsa dzanjalo, linali la khate lotuwa ngati ufa.

7-Chomcho AMBUYE adati, “Lipisenso m’malayamo dzanja lakolo.” Iye adalipisanso ndipo politulutsa, linali labwinobwino lopanda khate, koma lofanana ndi thupi lake lonse.

8-Pamenepo AMBUYE anati, “Akakapanda kukukhulupilira, usakachisamale chizindikiro choyambacho, akakhulupilira ndithu chifukwa cha chizindikiro cha chiŵiricho.

9-Koma akakapanda kukhulupilira zizindikiro ziŵiri zonsezo, osafuna kumva zomwe ukaŵawuzezo, ukatenge madzi a mu mtsinje wa Nayilo, ukaŵathire pa nthaka yowuma. Madzi amenewo akasanduka magazi.”

-Kodi chizindikiro choyamba chowonetsa kuti Mulungu anamusankha Mose kuti akaŵatsogolele a Isireyeli kutuluka mu Ejipito chinali chotani?

-Ndodo ya Mose inasanduka njoka, kenako inabweleranso kukhala ndodo.

-Kodi chizindikiro chachiŵiri chowonetsa kuti Mulungu anamusankha Mose kuti akaŵatsogolele a Isireyeli kutuluka mu Ejipito chinali chotani?

-Dzanja la Mose linasanduka kukhala la khate iye atalilowetsa m’mchovala mwake, ndipo linasandukanso



-Mulungu ndi wa mphamvu zonse.
-Palibe amene angathe kuchita zimene Mulungu angachite.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anali mchitsamba chimene chinkayakacho?
-Mulungu anali mchitsambacho kuti alankhulane ndi Mose za a Isirayeli.

-Kodi a Isirayeli ali bwanji ngati chitsamba chimene chinkayakacho?
-Satana ndi Farawo ankafuna kuŵawononga a Isirayeli ngati m’mene moto unkafunira kuwononga chitsamba chimene chinkayakacho.

-Mulungu anali ndi a Isirayeli ngati m’mene analili mchitsamba chimene chinkayakacho.

-Satana ndi Farawo sanakatha kuŵawononga a Isirayeli, Mulungu ali ndi iwowo.

-Mulungu anayitana dzina la Mose ali m’chitsamba chimene chinkayakacho.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 3:4

4-AMBUYE atawona kuto Mose akuyandikira, adamuyitana kuchokera mu chitsambamo kuti, “Mose, Mose!” Mose adayankha kuti, “ŵaŵa.”

-Mose sankadziŵa kuti Mulungu ali mchitsamba chimene chinkayakacho mpaka pa nthaŵI imene Mulungu analankhula kwa iye kuchokera mchitsambacho.

-Kodi Mulungu anachidziŵa bwanji chilankhulo cha Mose?
-Mulungu amazidziŵa zilankhulo zonse.

-Palibe chilankhulo chimene Mulungu sachidziŵa.

-Mulungu amachidziŵanso chilankhulo chanu.

-Mulungu amamva zonse zimene mumalankhula.
-Mulungu amamvetsa zonse zimene mumalankhula.

-Ngakhale kuti munong'one, Mulungu amamvabe chilichonse.

-Mulungu analankhulanso kwa Mose kuchokera mchitsamba muja.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 3:5-6

5-Mulungu adati, "Usayandikire pafupi. Vula nsapato zakozo, chifukwa chakuti pa malo pamene wayimapowo npoyera."
6-[Mulungu] adapitilira kunena kuti, "Ine Ndine Mulungu wa makolo ako, Mulungu wa Aburahamu, Mulungu wa Isaki, Mulungu wa Yakobo." Pompo Mose anadziphimba ku maso chifukwa chakuti adawopa kumuwona Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamuwuza Mose kuti avule nsapato zake?

-Chifukwa chakuti Mose anayipa pa maso pa Mulungu wabwino kwambiri.
-Chifukwa chakuti Mose anayima pa maso pa Mulungu woyera kwambiri.

-Kenako Mulungu anamuwuza Mose za a Isirayeli.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 3:7-10



-Kodi Mulungu anadziŵa bwanji kuti Farawo sakaŵalora a Isirayeli kuchoka mu Ejipito?
-Mulungu amadziŵa china chilichonse.

-Musanayambe kuganiza maganizo, Mulungu amakhala ataŵadziŵa kale maganizo anuwo.
-Musanalankhule liwu, Mulungu amakhala atalidziŵa kale liwu lanulo.

-Musanachite china chilichonse, Mulungu amakhala atachidziŵa kale chimene mukufuna kuchichitacho.

-Mose ankawopa kuti a Isirayeli sakamukhulupilirabe kuti Mulungu wamutumiza iye kuti adzaŵatsogolele iwowo kutuluka mu Ejipito.

-Apa pali zimene Mose analankhula kwa Mulungu.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 4:1

1-Mose adayankha kuti, "Koma a Isirayeliwo sakandikhulupilira, kapena kumvera mawu anga. Adzati, "AMBUYE sadakuwonekere."

-Chifukwa chakuti Mose ankawopa, Mulungu anamupatsa iye zizindikiro ziŵiri kuti akawonetse kwa a Isirayeli.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 4:2-9

2-AMBUYE adamufunsa Moseyo kuti, "Kodi ndi chiyani chimene chili m'manja mwakomo?" Mose adayankha kuti, "Ndodo."
3-AMBUYE adamuwuza kuti, "Tayiponya pansi." Mose atayiponya pansi ndodoyo, idasanduka njoka, iye nkumayithaŵa njokayo.

ndiye amene wanditumа kwa inu. Tsopano limeneli ndilo dzina Langa mpaka muyaya. Limeneli ndilo dzina limene idzanditchule mibado yonse ya mtsogolo.

16-Pita ukaŵasonkhanitse akuluakulu onse a a Isirayeli, ukaŵawuze kuti, “AMBUYE, Mulungu wa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo, adandiwonekera; adandilamula kuti ndikuwuzeni kuti wabwera kwa inu, ndipo zonse zimene akukuchitani a Ejipito, waziwona.

17-Mulungu watsimikiza kuti adzakutulutsani inu ku Ejipito kuno kumene mukuzunzika, ndipo adzakuloŵetsani m’dziko la a Kanani, a Hiti, a Amori, a Aperezi, a Hivi ndi a Ayebusi. Dzikolo ndi la mwana alilenji.”

18-Mulungu adapitilira kunena kuti, “Akuluakulu a a Isirayeli adzakumvera iwe.

-Mulungu anamuwuzanso Mose kuti akaŵawuze a Isirayeli kuti Mulungu wa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo wamutuma iye kuti akaŵapulumutse a Isirayeli kuchokera mu ukapolo.

-Kodi Farawo akaŵalora a Isirayele kuchoka ku Ejipito?

-Izi ndi zimene ananena Mulungu:

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 3:19-20

19-[Mulungu anati] “Kudziŵandikudziŵa kuti mfumu ya ku Ejipitoyo siyidzakulolani kuti mupite, mpaka nditayikakamiza kutero.

20-Tsopano ine ndidzagwiritsa ntchito mphamvu zanga ndipo ndidzalanga Ejipito ndi zozizwitsa zomwe ndidzachite kumeneko. Zikadzachitika zimenezo, adzakulorani.

-Mulungu ananena kuti Farawo sakaŵalola a Isirayeli kuchoka mu Ejipito.



7-Kenako AMBUYE anati, Ndawona m’mene anthu anga akuzunzikira ku Ejipito. Ndamva kulira kwawo kofuna chithandizo, chifukwa cha anthu amene akuŵapsinja. Ndikudziŵa bwino kuzunzika kwawo.

8-Ndabwera kuti ndiŵapulumutse kwa a Ejipitowo ndikuŵatulutsa m’dzikolo, kuti ndikaŵalowetse mu dziko lalikulu la chonde. Dziko limenelo ndi la mwana alirenji. Amene akukhala m’menemo ndi a Kanani, a Hiti, a Amori, a Aperezi, a Hivi ndi a Ayebusi.

9-Ine ndamva ndithu kulira kwa a Isirayele, ndipo ndaŵawonadi mazunzo amene a Ejipito akuŵapsinja nawo.

10-Tsopano iwe ndikukutuma kwa Farawo kuti ukaŵatulutse anthu anga a Isilayeli ku Ejipito.”

-Mulungu anamuwuza Mose kuti wamva kulira kwa a Isirayeli.

-Mulungu anamuwuza Mose kuti amusankha iye kuti akaŵatsogolele a Isirayeli potuluka mu Ejipito mu ukapolo.

-Mulungu anamuwuza Mose kuti amusankha iye kuti akaŵatsogolele a Isilayeli pobwerera ku dziko la Kanani.

-Kodi Mose anayankha chiyani kwa Mulungu?

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 3:11

11-Apo Mose anafunsa kuti, “Kodi ine ndi ndani ine, kuti ndingapite kwa Farawo ndikukaŵatulutsa a Isirayele ku Ejipito?”

-Mose anamuwuza Mulungu kuti iye sangathe kukaŵatsogolera a Isirayeli kutuluka mu Ejipito.

-Kodi chifukwa chiyani Mose anamuwuza Mulungu kuti iye sangathe kuŵatsogolera a Isirayeli kutuluka mu Ejipito?

-Chifukwa chakuti Mose anayikumbukira nthaŵI yimene anayesa kuti aŵathandize a Isirayeli , koma analephera.

-Kodi Mulungu anayankha chiyani kwa Mose?

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 3:12

12- Mulungu anamuyankha kuti, "Ine ndidzakhala nawe. Chitsimikizo chakuti ndakutuma ndi Ine ndi ichi: Ukadzaŵatulutsa anthu anga ku Ejipito, mudzandi-pembedza pa phiri lomwe lino."

-Mulungu anamuwuza Mose kuti adzakhala ndi iye.
-Mulungu anamupatsa Mose chizindikiro.

-Kodi chizindikiro chimene Mulungu anapereka kwa Mose chinali chotani?

-Mulungu anamulonjeza Mose kuti adzamubweretsanso Mose pa phiri limene anawona chitsamba chikuyakalo.

-Dzina la phirilo linali Phiri la Sinayi.
-Kodi Mose anayankha chiyani kwa Mulungu?

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 3:13

13-Mose adayankha kuti, "Tsopano ine ndikapita kwa a Isirayeli ndikukaŵawuza kuti Mulungu wa makolo anu wandituma kwa inu, iwowo akakandifunsa kuti, "Dzina lake ndani?" Ndiye ineyo ndakaŵawuze chiyani?"



-Mose ankawopa kuti a Isirayeli sakamukhulupilira iye aka-kaŵawuza kuti Mulungu wamutumiza iye kuti adzaŵapu-lumutse iwowo kuchokera mu ukapolo.

-Chomcho, Mose anamufunsa Mulungu Dzina Lake limene akaŵawuze a Isirayeli.

-Kodi Mulungu ayankha bwanji?

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 3:14

14-Mulungu anamuwuza kuti, "Dzina langa ndine NDILIPO. A Isirayeliwo ukaŵawuze kuti, NDILIPO wandi-tuma kwa inu."

-Mulungu anamuwuza Mose kuti akaŵawuze a Isirayeli kuti "NDILIPO" wamutumiza Mose kuti akaŵapulumutse a Isilayeli mu ukapolo.

-Kodi dzina lakuti "NDILIPO" likuthandawuza chiyani?

-Limatanthandawuza kuti Mulungu alibe chiyambi.
-Limathandawuza kuti Mulungu alibe mathelo.

-Limatanthawuza kuti Mulungu wakhala alipo nthaŵI zonse.
-Limatanthawuza kuti palibe nthaŵI imene Mulungu kunalibe.

-Mulungu analankhulanso izi kwa Mose:

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 3:15-18a

15-Ndipo Mulungu anamuwuza Mose kuti, "A Isirayeli ukaŵawuze kuti, AMBUYE, Mulungu wa Aburahamu , Mulungu wa Isaki, Mulungu wa Yakobo,